




MUTU 5:

*ANENERI*

---




TIKUPEREKA MWANA  
WOSALAKWAYU KWA INU,  
BAALA. LOLANI KUTI  
MAGAZI AKE AZIME  
MKWIYO WANU.

NDIPEREKA  
MWANA WANGA  
CHIFUKWA CHA  
MACHIMO  
AMENE  
NDACHITA.

ANTHU AMENE ANKAKHALA M'DZIKO  
LA PALESTINA, DZIKO LIMENE ANA  
A ISRAELE ANALOWAMO, ANALI  
OIPA. ANTHUWO ANKATCHEDWA  
AKANANI NDIPO ANALI A ZIYANKHULO  
ZOSIYANASIYANA, CHONCHO  
SANKAFANANA NDI AISRAELE.  
ANKAPEREKA NSEMBE ANTHU  
ANZAO KOMANSO ANKAGWADIRA  
MILINGU YOPANGIDWA NDI GOLIDE,  
SILIVA, MKUWA, NDI MITENGO.

MULINGU ANATUMIZA ANENERI  
NDI ANSEMBE KUTI AWACHENJEZE  
ZA KUTEMBENUKA MTIMA, KOMA  
ANAPITIRIRABE KUCHIMWA. MONGA  
MOMWE MULINGU ANAONONGERA  
ANTHU A PA NTHAWI YA NOWA  
NDI MIZINDA YA SODOMU NDI  
GOMORA, MOMWEMO ANAFUNANSO  
KUONONGA ANTHU A KU KANANI.




TSIKU LINA  
NAFENSO TIDZAKHALA  
AKULU A ANSEMBE,  
NDIPO NDIFE AMENE  
TIZIDZAPEREKA  
NSEMBE.

SIZABWINO,  
KOMABE ZIYENERA  
KUCHITIKA. CHITANI  
ZABWINO KUTI  
MULANDIRE ZABWINO;  
CHITANI ZOIPA KUTI  
MULANDIRE ZOIPA.




ANTHU OPEMBEDZA MAFANO A M'DZIKO  
LAMALONJEZANO SANKAFUNA AISRAELE  
M'DZIKOMO NDIPO ANKACHITA NAWO  
NKHONDO POFUNA KUSUNGA DZIKO LAO.  
KOMA MULLINGU ADAAPATSA MPHAMVU ANA  
A ISRAELE KUTI AGONJETSE ADANI AOWO.



**WABWERA  
BWANJI  
M'KACHISI  
WOPATULIKA  
LINO?**

**MWAPHA  
MWANA  
WANU  
WOMALIZA.**



ITATHA NKHONDO YOOPSAYO,  
AHEBRI ANAPAMBANA ADANI AO,  
NDIPO DZIKOLO LINAKHALA  
M'MANJA MWAO. YOSWA  
ANAYANKHULA NDI AISRAELEWO.

GOGO WATHU,  
ABRAHAMU ANACHOKERA PAKATI  
PA ANTHU OPEMBEDZA MAFANO.  
MULINGU ANAYANKHULA NAYE  
NDIPO ANAMULONJEZA KUTI  
ADZAMSANDUTSA MTUNDU  
WAIKULU.



.// MULLINGU  
ANANENANSO KUTI ANTHU  
AKE ADZAPITA KU IGUPTO  
KUMENE AKAKHALEKO ZAKA 400,  
PAMBUIYO PAKE ADZAWATULUTSA  
NDI KUWABWEZERA KU DZIKO  
LINO LIMENE INU MUKUKHALAMO  
TSOPANO. TAONANI, KWA ZAKA  
ZOPITIRIRA 500, MULLINGU  
WASUNGA MALONJEZANO AKE  
KWA ABRAHAMU. // TSOPANO  
PITANI NDI KUKAKHALA PALIPONSE  
M'DZIKO LINO. MUSATENGERE  
MAKHALIDWE A ANTHUOCHIMWA  
AMENE ANKAKHALA M'DZIKO  
LINO INU MUSANABWEREMO,  
CHIFUKWAMULLINGUADZAKUWER  
LIZANI MONGA WAWERUZIRA  
IWOWO.

M'DZIKO LATSOPANOLO ANALI  
PA MTENDERE. ALIYENSE ANALI  
NDI MUNDA WAKE NDIPO ANALI  
NDI CHAKUDYA CHAMBIRI.  
MULINGU ANAWADALITSA  
KUPOSA ANTHU ENA ONSE.



CHAKUDYA  
CHANU  
CHAKONZE  
DWA.

TIKANGOTENGA  
ICHOCHO  
MUTSEKE





MTENDERE  
UKHALE NAWA,  
MLONGO  
WANGA. KODI  
NSOMBAZI ZILI  
BWINOBWINO?

MONGA MOMWE MULLINGU ANALONJEZERA,  
AHEBRI ANACHULLUKANA KWAMBIRI MPAKA  
ANADZAZA DZIKOLO. MIZINDA YAO  
INKACHITA BWINO CHIFUKWA CHOFUNIRANA  
ZABWINO NDI CHILINGAMO. DZIKO  
LATSOPANOLO LINKATCHEDWA ISRAELE.


ZILI BWINOBWINO  
MONGA MWA  
NTHAWI ZONSE  
POPEZA  
ZIKUNGOCHOKERA KU  
NYANJA KUMENE.



YHOVA WAGONJETA ADANI ANU, KOMA  
KUPEMBEDZA MAFANO KUKANALIPO M'DZIKO  
MUNO. SANKHANI LERO AMENE MUDZAMTUMIKIRA;  
KAPENA MILINGU YABODZA YA ANTHU A M'DZIKO  
LIMENE MUKUKHALALI, KAPENA MULINGU WA  
ABRAHAMU. KOMA INE NDI BANJA LANGA,  
TIDZATUMIKIRA AMBUYE.



NZOSATHEKA KUTI IFE TISIYE  
AMBUYE NDI KUTUMIKIRA MILINGU INA;  
POPEZA NDI MPHAMVU ZAKE ZAZIKULU  
YHOVA ANATITULUTSA MU UKAPOLO  
M'DZIKO LA IGUPTO NDIPO  
ANATISAMALIRA M'CHIPULULU.



NDIPO AMBUYE ANATITHAMANGITSIRA  
ANTHU ONSE, NGAKHALE AAMORI AMENE  
ANKAKHALA M'DZIKO LINO. CHONCHO  
IFENSO TIDZATUMIKIRA AMBUYE; POPEZA  
IYEYO NDI MULLINGU WATHU.



MULINGU NDI WOYERA;  
NDI MULINGU WANSANJE;  
MUKAMUSIYA NDI KUTSATA  
MAFANO, ADZAKUONONGANI  
NDIPO ADZAKUTHANI PSITI.

TIKULONJEZA  
KUTUMIKIRA  
AMBUYE.



INU ENI AKE NDINU MBONI KUTI  
MWASANKHA KUTUMIKIRA AMBUYE.

NDIFE MBONI.

NDILEMBA M'BUKU PANGANO  
LIMENE MWACHITA NDI  
MULLINGU LERO LINO.

TINKAMVERA MOSE PA ZINTHU ZONSE,  
TIDZAKUMVERANINSO INUYO; KOMA AMBUYE MULLINGU  
WANU AKHALE NANU, MONGA ANKACHITIRA NDI MOSE.  
ALIYENSE AMENE ADZAGALUKIRA MALAMULO A  
MULLINGU ADZAPHEDWA.

ANTHUWO ANKALAMULIDWA NDI OWERUZA  
AMENE AMAYANKHULA NDI MULLINGU  
NDIPO ANKAWERENGA MALAMULO A  
MOSE. ANKAFOTOKOZERA ANTHUWO ZA  
MALAMULO A MULLINGU NDI KUWALIZA  
KUTI AZIMVERA MULLINGU.



MOSE ANATI MWINI  
NG'OMBEO ABWEZERE  
ZIMENE ZAONONGEKAZO  
NDIPO NG'OMBEO  
IPHEDWE.



KODI MALAMULO  
A MULLINGU AMATI  
CHIYANI PA ZA  
NG'OMBE IMENE  
YAGUNDA MUNTHU?

EKSODO 21:28-29; YOSWA 24:15-24




KWA KANTHAWI, ANTHU ANAKUMBUKIRABE  
ZUZIZWITSA ZIMENE MULLINGU ANACHITA  
KUPYOLERA MWA MOSE NDI AARONI.  
ANKAYAMIKA CHIFUKWA CHA KUTULUKA MU  
LUKAPOLO WA KU IGUPTO. ANKATUMIKIRA  
YEHOVA MULLINGU NDIPO ANKAPEREKA  
NSEMBE ZIMENE ANALAMULIDWA.





ABABA, KODI  
ANSEMBE AFUNA  
KUPHERANJIMWANAWANKH  
OSA WATHUYU? KODI  
MNGELO WOONONGA UJA  
ADUTSA MONGA ANACHITIRA  
NDI MAKOLO ATHU KU  
IGUPTO?

AI MWANA WANGA,  
WOONONGAYO SABWERA,  
KOMA MAGAZI A  
MWANAWANKHOSAYU  
ADZACHOTSA MACHIMO  
ATHU NDIPO TIDZAKHALA  
OVOMEREZEKA PAMASO  
PA MULLINGU.



ADALONJEZA YOSWA KUTI  
ADZAPEMBEDZA MULLINGU NDI  
KUSUNGA MALAMULO AKE, KOMA  
SI ONSE AMENE  
ANKAPEMBEDZABE YEHOVA.

PAMENE ZOZIZWITSA ZINALEKA  
KUONEKA, MBADWO WINAWO UNAIWALA  
MULLINGU WAMOYO NDIPO  
UNKAPEMBEDZA MAFANO OPANDA MOYO.  
ANKAPEMBEDZANSO MAKOLO AO.


MONGA MOMWE YOSWA  
ANAWACHENJEZERA,  
MULLINGU ANATUMA  
ANTHU AKUNJA KUTI  
AONONGE ISRAELE.

**PULUMUTSENI  
BAALA!**

**AAAAAAA!**

OWERUZA 3:7-8, 12-13, 4:1-2, 10:6-7






ANTHU A MULLINGUWO AKAONA  
CHILANGO, ANKAKUMBUKIRA  
MALAMULO AKE NDI  
KUVOMEREZA MACHIMO AO.

O YEHOVA,  
TIKHULULUKIRENI  
MACHIMO ATHU NDI  
KUTIBWEZERA MTENDERE  
WATHU.

AKAVOMEREZA MACHIMO AO,  
ANKAWAKHULULUKIRA NDI  
KIWABWEZERA DZIKO LAO.



ANTHU AJA ANATOPA NDI  
OWERUZA CHIFUKWA CHA  
ZOCHITA ZAO NDIPO ANAGANIZA  
ZOKHALA NDI MFUMU KUTI  
NDIYO IZIWALAMULIRA.

TIDZALANDA MINDA  
YANU KUTI UFUMU  
UZIYENDA BWINO. SIYANI  
MWANA WANU KUNO.  
TIDZAMUSAMALIRA.



MNERI AMENESO ANALI OWERUZA,  
DZINA LAKE SAMUELE, ANAWACHENJEZA  
KUTI AKAFUNA KUKHALA NDI MFUMU  
NDIYE KUTI AKUKANA MULLINGU AMENE  
AMAWALAMULIRA, KOMA ANTHUWO  
SANKAFUNA KUYENDA M'CHIKHULUPIRIRO.  
MFUMU SAULI ANAWACHITIRA ZACHABE,  
ANAWALANDA NDALAMA, CHUMA CHAO,  
NDIPO ANA AO AAMUNA  
ANAWASANDUTSA AKAPOLO, ANA AO  
AAKAZI ANAWACHITIRA ZAMANYAZI.





TSIKU LINA, ANAFUNA KUPHA  
NDI MKONDO MNYAMATA WINA  
WOTCHEDWA DAVIDE AMENE  
ANKAMUIMBIRA ZEZE.

MFUMU SAULI ATAKALAMBA,  
MIZIMU YOIPA INAMULOWA  
NDIPO ANKAKWIYA KWAMBIRI.



SAULI ANKANGOCHIMWIRACHIMWIRA.  
ANKACHITA NSANJE NDI WINA  
ALYENSE NDIPO ANKAKHALA  
MWAMANTHA. MIZIMU YOIPA  
INAMULONJEZA KUMPATSA  
MPHAMVU NDI CHUMA, KOMA  
INAMUBWERETSERA MAVUTO NDI  
MAZUNZO PA MOYO WAKE.



NDIKLONA MDIMA.  
SIZABWINO. UDZAFERA  
KU NKHONDO NDIPO  
WINA ADZALAMULIRA  
M'MALO MWAKO.

SAULI ANASIYA  
MULLINGU WAMOYO  
NDIPO ANKAFUNSIRA  
NZERU KWA AFITI.

SAULI ANAFERA KU NKHONDO  
NDIPO MZIMU WAKE UNAPITA  
KU CHIONONGEKO.





1 SAMUELE 18:10-11, 31:4,  
16:1-13; MASALIMO 23:1-3

CHALTA NDIYE MBUSA  
WANGA SINDIDZASOWA  
KANTHU. AMANDIGONEKA  
PA BUSA LA MSIPLU.  
AMATSITSIMUTSA  
MOYO WANGA.

MULLINGU ANASANKHA  
MNYAMATA KUTI ALAMULIRE  
M'MALO MWA SAULI. ANALI  
MBUSA WA ZIWETO AMENE  
ANKAKONDA MULLINGU NDI  
KUSUNGA MALAMULO AKE;  
MUNTHU AMENE SAULI  
ANAFUNA KUMUPHA.


DAVIDE ANALI MUNTHU WOLINGAMA  
NDIPO MULLINGU ANKAMUKONDA.  
KODI NDIYE ADZAPULUMUTSE ANTHU  
KU MACHIMO NDI KU IMFA? KODI  
DAVIDE ADZAKHALA MPULUMUTSI  
WOLONJEZEDWA UJA?



DAVIDE ANKAKONDA  
KUIMBIRA  
MULINGU NDIPO  
ADAALEMBA  
NYIMBO ZAMBIRI.

DAVIDE ADALEMBA: NGODALA MUNTHU  
WOSATSATA UPHUNGU WA ANTHU OIPA,  
WOSATSANZIRA MAYENDEDWE A ANTHU  
OCHIMWA, WOSAKHALA NAWO M'GULU  
LA ANTHU ONYOZA MULINGU, KOMA  
WOKONDWERERA KUMVERA MALAMULO  
A CHAUTA, NKUMASINKHASINKHA ZA  
MALAMULOWO USANA NDI USIKU. MUNTHUYO  
ALI NGATI MTENGO WOBZALIDWA M'MBALI  
MWA MTSINJE WA MADZI, NGATI MTENGO  
WOBEREKA ZIPATSO PA NTHAWI YAKE, UMENE  
MASAMBA AKE SAFOTA KONSE. ZOCHITA ZAKE  
ZONSE ZIMAMUYENDERA BWINO. ANTHU  
OIPA SALI CHONCHO, ALI NGATI MUNGU  
WOULLZIKA NDI MPHEPO. NCHIFUKWA CHAKE  
ANTHU OCHIMWA MULINGU ADZAWAZENGA  
MLANDU, ADZAWACHOTSA PAKATI PA ANTHU  
AKE. PAJA CHAUTA AMAWASAMALIRA ANTHU  
AKE, KOMA ANTHU OCHIMWA ADZAONONGEKA.


SAULI ATAMWALIRA, DAVIDE  
ADAKHALA MFUMU YA AISRAELE,  
NDIPO ADAPHUNZITSA AISRAELE  
KUPEMBEDZA MULLINGU NDI  
KUSUNGA MALAMULO AKE.



MUMUBWEZERE  
MALO AKE MAIYU  
NDIPO MUONETSETSE  
KUTI ASAMAKHOMENSO  
MSONKHO.

PA NTHAWI IMENE  
DAVIDE ANALI MFUMU  
DZIKOLO LINATUKUKA  
NDIPO LINKACHITA  
CHILINGAMO.

2 SAMUELE 2:4; MASALIMO  
1; MACHITIDWE 13:22-23



MULUNGU ANKAYANKHULA NDI DAVIDE  
NDIPO ANAMULIRA ZINSINSI ZAMBIRI  
ZONENA ZA M'TSOGOLO. DAVIDE  
ANALEMBA MAVUMBULITSOWO M'BUKU LA  
MASALIMO. AMBIRI MWA  
MAVUMBULITSOWO AKWANIRITSIDWA KALE.



MFUMUYO IDZAWERUZA ANTHU ANU  
MOLUNGAMA, NDIPONSO ANTHU ANU  
OSAIKA MOSAKONDERA. IDZATETEZA  
ANTHU OSAIKA, IDZAPULUMUTSA ANTHU  
OSOWA, KOMA IDZAONONGA ANTHU  
OZUNZA ANZAO. PA MASIKU AKE  
CHILINGAMO CHIDZAKULA, MTENDERE  
UDZACHULLIKA MPAKA MWEZI UTALEKA  
KUWALA! IDZAKHALA IKULAMULIRA  
KUCHOKERA KU NYANJA INA MPAKA KU  
NYANJA INA, KUCHOKERANSO KU MTSINJE  
MPAKA KU MATHERO A DZIKO. MAFUMU  
ONSE ADZAIGWADIRA NDIPO MITUNDU  
YONSE YA ANTHU IDZAITUMIKIRA.  
OWAPSINJA NDI KWA OWACHITA  
ZANKHANZA: IKHALE NDI MOYO WAUTALI.  
ANTHU AIPEMPHERERE NTHAWI ZONSE;  
AIPEMPHERERE MADALITSO KOSALEKEZA.




OWAPSINJA NDI KWA OWACHITA  
ZANKHANZA: IKHALE  
NDI MOYO WAUTALI.  
ANTHU AIPEMPHERERE  
NTHAWI ZONSE;  
AIPEMPHERERE MADALITSO  
KOSALEKEZA.  
DZINA LAKE LISAIWALIKE  
KONSE: MBIRI YAKE  
IKHALEPOBE MONGA  
MOMWE LIMAKHALIRA  
DZUWA. ANTHU ALANDIRE  
MADALITSO  
CHIFUKWA CHA IYO,  
ANTHU A MITUNDU  
YONSE AITCHE YODALA.

(MASALIMO 72)

**MULLINGU ANATI KWA DAVIDE:  
LIKADZABA, NDIDZAKHAZIKITSA  
UFUMU WAKO MWA MWANA WAKO  
WAMWAMLINA. ADZAMANGA KACHISI  
AMENE AZIDZANDIPEMBEDZERAMO,  
NDIPO INE NDIDZAKHAZIKITSA  
UFUMU WAKE MPAKA KALEKALE.**

**DAVIDE ATAFU, SOLOMO ANALOWA UFUMU  
M'MALO MWAKE (971 B.C.). MONGA MMENE  
MULLINGU ADANENERA KWA DAVIDE, SOLOMO  
ANAMANGA KACHISI (966 B.C.) KULOWA M'MALO  
MWA CHIHEMA CHAKALEKALE CHIMENE  
CHINKAGWIRITSIDWA NTCHITO M'CHIPULULU.  
AISRAELE ANATUKUKA KUPOSA KALE. ZONADI,  
MULLINGU ANAKWANIRITSA MALONJEZO AKE KUTI  
ADZAWALOWETSA M'DZIKOMO NDI KUWADALITSA.**





KOMA PANALI LONJEZO LIMODZI LIMENE  
MULLINGU ANALI ASAKWANIRITSEBE - KUBWERA  
KWA MPULUMUTSI AMENE ATI ADZAONONGE  
NTCHITO ZA SATANA. ANTHU ANKACHIMWABE  
NDIPO MAGAZI A NYAMA ANKAPEREKEDWA  
CHIFUKWA CHA MACHIMO AO. KOMABE  
ANKAYAMIKA CHIFUKWA MULLINGU ADAKONZA  
NJIRA YOKHULULUKIRA MACHIMO AO KUFIKIRA  
PAMENE MPULUMUTSI ADZABWERE  
KUDZACHOTSERATU MACHIMO ONSE.

2 SAMUELE 7:12-16;  
MASALIMO 72:1-20



ANTHU ANKABWERA KU KACHISI KUDZAMVA  
MAPHUNZITSO A M'MALEMBO OPATULIKA.  
MAKAMAKA ANKAKONDWERA NDI MALINENERI  
OKHUDZA ZA KUBWERA KWA MPULUMUTSI.



*AMBUYE WALLUMBIRA MONENETSA KWA DAVIDE;  
SADZALEKA KUCHITA ZIMENE WANENAZO;  
MMODZI MWA ZIPATSO ZA M'THUPI MWAKO  
NDIDZAMUIKA PA MPANDO WAKO. NDIWE  
MWANA WANGA; LERO NDAKLIBALA IWE.  
PSOPSONANI MWANA KUTI ANGAKWIYE NDI  
KUKUONONGANI M'NJIRAYO PAMENE  
MKWIYO WAKE LIYAKA KOMA KWA  
KANTHAWI KOCHAPA CHABE.*

DAVIDE ANALEMBA ZINTHU ZAMBIRI  
ZOKHUDZA MPULUMUTSI WODZABWERAYO:  
CHAITA ADAIZA MBUYE WANGA KUTI, KHALA  
KU DZANJA LANGA LAMANJA, MPAKA  
NDITASANDUTSA ADANI AKO KUKHALA NGATI  
CHOPONDAPO MAPAZI AKO  
(SALIMO 110:1).

MPANDO WANU WAUFUMU,  
INU MULUNGU, NDI WAMUYAYA,  
MUMAWERUZA MOLLINGAMA MU UFUMU  
WANU. MUMAKONDA CHILUNGAMO NDIPO  
MUMADANA NDI ZOIPA. NCHIFUKWA CHAKE  
MULUNGU, MULUNGU WANU,  
WAKUSANKHANI. WAKUDZOZANI NDI  
KUKUSANGALATSANI KUPAMBANA  
ANZANU ENA ONSE  
(SALIMO 45:6-7).



MAULOSI ENA AMBIRI OKHUDZA  
MPULUMUTSI WODZABWERAYO:

NDITHU NDIDZAMSANDUTSA MWANA WANGA  
WACHISAMBA, ADZAKHALA WOPAMBANA MAFUMU  
A DZIKO LAPANSI  
(SALIMO 89:26-27).

NDIMAKONDA KUCHITA ZIMENE MUMAFUNA,  
INU MULLINGU WANGA, MALAMULO ANU ALI  
MUMTIMA MWANGA  
(SALIMO 40:8).

NDIDZAKUSIMBIRANI FANIZO.  
NDIDZAYANKHULA NKHANI ZOBISIKA  
ZAKALEKALE  
(SALIMO 78:2).

DAVIDE ANALEMBA CHINTHU CHINA  
CHODABWITSA CHOKHUDZA  
WODZOZEDWA WODZABWERAYO:

MOYO WANGA WATAYIKA NGATI  
MADZI, MAFUPA ANGA AWEYESEKA.  
MTIMA WANGA ULI NGATI SERA,  
WASUNGUNUKA M'KATI MWANGA.  
KUKHOSI KWANGA KWALUMA NGATI  
PHALE, LILIME LANGA LAKANGAMIRA  
KU NSAGWADA. INU MWANDISIYA PA  
FUMBI KUTI NDIFERE POMWEPO.  
ANTHU ANKHANZA ANDIZINGA NGATI  
MIMBULLI. ABOOLA MANJA ANGA NDI  
MAPAZI ANGA. MAFUPA ANGA  
AKUWONEKERA, KOMA ANTHU AJA  
AKUNGONDIYANG'ANITSITSA,  
AKUKONDWERA POONA KUTI  
NDIKUVUTIKA. AGAWANA ZOVALA  
ZANGA, NDIPO ACHITIRA MALAYA  
ANGA MAERE.  
(SALIMO 22:14-18).

SOLOMO ADALAMULIRA NTHAWI YAITALI NDIPO UFUMU WAKE UDATUKUKA KWAMBIRI, KOMA ATAMWALIRA THEKA LA UFUMU WAKE LIDAMUCHOKERA NKULONGA UFUMU MUNTHU WOIPA DZINA LAKE YEROBOWAMU (975 B.C.).

UYU NDI MULLINGU AMENE ANAKUTULITSANI KU IGUPTO, NDIPO AWA NDI ANSEMBE AKE.

KOMA NANGA ZA MALAMULO A MOSE NDI KACHISI AMENE MULLINGU ANAKHAZIKITSA KU YERUSALEMU?

1 MAFUMU 12:20, 28:29; MASALIMO 2:7, 12, 22:6, 14-18, 40:8, 78:2, 45:6-7, 89:26-27, 110:1, 4, 132:11

UFUMU WA KUMPOTO UDALI KUTALI NDI KACHISI WA KU YERUSALEMU, NDIPO ANTHUWO ADAMANGA MALO AOAO ACHIPEMBEDZO, NKUIKAMO MAFANO A ANAANG'OMBE A GOLIDE.

PALI NJIRA ZAMBIRI ZOPITIRA KWA MULLINGU. ENA AMAMUTCHULA KUTI YEHOVA, ENA AMAMUTCHULA KUTI ALA, ENA AMAMUTCHULA KUTI KEMOSI, KOMA IFE TIMAMUTCHULA KUTI BAALA.

KOMA NANGA ZA MALEMBO OYERA AMENE MULLINGU ANAPEREKA KWA ANENERI AKE? MAUWO AMATILANGIZA KUTI TISAKHALE NDI MILLINGU INA. CHONCHO MALEMBOWO AMATI MULLINGU NDI MMODZI NDIPO NJIRA YOPITIRA KWA IYE NDI IMODZINSO.






**KODI MUKUGANIZA  
KUTI MULUNGU WATHU  
NDI WOPEPERA?**

**SINDIKUFUNA KUMVANSO  
ZIMENEZI! CHIPEMBEDZO CHA  
BAALA NDICHO CHIPEMBEDZO  
CHIMENE ALIYENSE AYENERA  
KUTSATIRA M'DZIKO MUNO.  
WONYOZERA ADZAPHEDWA!**

PAMENE ANSEMBE ADASANKHA FANO LA NG'OMBE LOTI  
AZILIPEMBEDZA SANAZINDIKIRE KUTI ADASANKHA FANO LENILENI LA  
LUSIFARA, MNGELO WOCHIMWA UJA. ANKAPEMBEDZA SATANA, NDIPO  
SATANAYO ANKASANGALALA, POPEZA ANKACHITITSA KUTI ANTHUWO  
AGALLUKIRE MULLINGU PA ZA MPULUMUTSI WODZABWERAYO.



INU BAALA,  
LANDIRANI NSEMBE  
IYI KUCHOKERA  
M'MANJA MWATHU  
MWACHABECHABEMU.

WODALITSIKA  
NDINU MFUMUKAZI  
YA KUMWAMBA, MAI  
WA MULLINGU, IMVANI  
MAPEMPHERO ATHU  
NDIPO  
MUTIKHULLULUKIRE  
MACHIMO ATHU.




A comic book illustration of a scene. In the center, a large, ornate metal fire pit sits on a stand, with bright yellow and orange flames rising from it. To the left, a man with a long white beard and a white robe with gold trim and a gold sash stands looking towards the right. To the right, another man with a long white beard and a dark robe is seen from the back, looking towards the first man. The background is a simple, warm-toned interior with a wooden floor and a doorway in the distance. A large speech bubble is positioned in the lower half of the image, containing text in both Shona and English. Another smaller speech bubble is positioned above the first man, containing a question in Shona.

MUKUCHITA  
CHIYANI PA MALO  
OYERAWO?

M'DZINA LA **YEHOVA**, AMENE INU  
MWAMUGALUKIRA, IMVANI MAU A AMBUYE. MWANA  
ADZABADWA KUCHOKERA MWA ZIDZUKULU ZA DAVIDE.  
MPULLUMUTSI ADZABWERA KUCHOKERA MU MBADWO  
WA DAVIDE. DZINA LAKE ADZATCHEDWA YOSIYA,  
NDIPO PA GUWA LANSEMBE ILI ADZAOTCHERAPO  
ANSEMBE A BAALA.

1 MAFUMU  
12:28, 13:1-2;  
YEREMIYA  
44:17-25



UNGANENE BWANJI  
ZIMENEZO? PALIBE  
AMENE ANGANENE  
ZAKUTSOGOLO KOMA  
MILINGU YOKHA.

MWA MAU A AMBUYE  
NDIKUNENA KWA INU KUTI  
YOSIYA ADZATENTHA MAFUPA  
A ANENERIWA PA GLUWA  
LANSEMBE ILI.



MULINGU ADZAKUPATSANI  
CHIZINDIKIRO CHAKUTI INE  
NDIKUYANKHULA M'MALO MWAKE.  
LERO LOMWE LINO GUWA  
LOSALALALO LIMENE MWAMANGA  
KUTI MUZIPEMBEDZERAPO MAFANO  
OSAYANKHULA LING'AMBIKA NDIPO  
PHULUSA LITULUKIRA KUNJA.

HA, HA, HA, TAMVANI  
ZIMENE AKUNENA MUNTHU  
WOPUSAYU. AKUGANIZA KUTI  
IYE YEKHA NDIYE AKUCHITA  
BWINO NDIPO KUTI  
ALIYENSE NGOLAKWA!




MGWIRENI! MUPHENI.  
ANGAYANKHULE  
BWANJI ZOTSUTSANA  
NDI CHIPEMBEDZO  
CHA ENA!

**DZANJA LANGA  
LAPUWALA! YEHOVA  
WANDILANGA. PEMPHERA  
KUTI ANDICHIRITSE.**





AMBUYE MULLINGU,  
DZIULULENI NOKHA  
LERO LINO. CHIRITSANI  
MKONO WA MFLUMUYI.



NDI CHODABWITSA  
NDITHU! MULLINGU  
WACHIRITSA  
MKONO WANGA!

1 MAFUMU 13:2-6

**THII!**


**VUUU!**

**EEEEEEEEEE!**

**AAAAA!**


**YHOVA  
WAYANKHULA!**





ZOONADI IWE NDIWE MUNTHU WA MULLINGU! PALIBE MNENERI WA BAALA AMENE ADACHITAPO ZOTERE. NDITSATE. TIYE TIKADYE CHAKUDYA NDI KUMWA CHAKUMWA NDIPO NDIDZAKUPATSA CHUMA NDI ULEMERERO CHIFUKWA CHA NTCHITO YAIKULU IMENE WAGWIRIRAYEHOVA LERO LINO.

AI, SINDINGAKUTSATENI. PAMENE NDINALI KU YUDA MULLINGU ADANDIENZA KUTI NDISADYE KAPENA KUMWA NGAKHALE MADZI, ANATINSO NDISADZERE NJIRA YOMWE NDINADZERA POBWERA KUNO.



WAONONGA  
CHIPEMBEDZO  
CHANGA. PALIBE  
CHIMENE  
CHATSALAPO.


ANALI MAU A MULLINGU,  
OSATI ANGA. INENSO SINDIKUDZIWA.  
NDINGODZIWA KUTI NDI MULLINGU  
AMENE ANAYANKHULA, OSATI INE.

KOMA UNATI  
MAFUPA A ANSEMBE  
ADZATENTHEDWA PA  
GUWALI. GUWA  
LAONONGEKA NDIPO  
PALIBE AMENE WAFWA.

1 MAFUMU 13:5, 7-9

CHONCHO MONGA MOMWE MULLINGU  
ADALAMULIRA, MNENERI WA MULLINGU  
UJA ANABWERERA PODZERA NJIRA INA.  
SADADYE KAPENA KUMWA CHILICHONSE  
PA MASIKU AWIRI NDIPO ANAVUTIKA  
KWAMBIRI NDI LUDZU KOMANSO NJALA.  
ANYAMATA AWIRI, AMENE  
ANKAPEMBEDZA FANO LA NG'OMBE LA  
GOLIDE PA TSIKULO, ANAMUTSATIRA KUTI  
AWONE KUMENE MNENERIYO ANKAPITA.






**ATATE,  
SINDIKANAKH  
ULLUPIRIRA  
NDIKANAPAND  
A KUONA  
ZIMENE ZIJA.  
ANALI NGATI  
MNENERI  
WAKALELO KU  
ISRAELE!**

**ATATE, MUKUGANIZA  
KUTI ZIMENE AMANENA  
ZIJA NDI ZOONA? KODI  
YEHOVA YEKHA NDIYE  
MULINGU WAMOYO? KODI  
MAFANO ATHUWA SIKANTHU  
KOMA NDI MITENGO NDI  
GOLIDE BASI?**

**FULUMIRA!  
KWERA BULLUYU!  
NDIYENERA  
KUMPEZA BASI!**



ADAMUPEZA MNENERI WA MULLINGU UJA  
ATAKHALA PANSI PA MTENGO. ADAFUNA KUTI  
AKHALE BWENZI LA MUNTHU WAMPHAMVUYO.  
ADALIPO MNENERI WA YEHOVA KALELO, KOMA  
PAMENE UFUNU UNAGAWANIKA, ANAYAMBA  
KUTSATIRA MAFANO A ANTHU A M'DZIKO  
MWAKE. KENAKA ANAYAMBA KUGANIZA KUTI,  
"KODI ZIPEMBEDZO ZONSE SIZOFANANA?"




NDIYESA KUTI NDIWE MUNTHU WA MULLINGU  
WOCHOKERA KU YUDA. UKUONEKA KUTI WATOPA.  
TIYE KUNYUMBA KWANGA KUTI NDIKAKUPATSE  
CHAKUDYA NDI CHAKUMWA.

SINDINGATERO,  
MULLINGU  
ANANDIENZA KUTI  
NDIKAFIKA KUNO  
NDISADYE KAPENA  
KUMWA.

AMBUYE  
ALEMEKEZEKE,  
NDILI NDI LUDZU  
KWAMBIRI.

UKUDZIWA, INENSOTU  
NDINE MNENERI MONGA  
IWEYO, NDIPO LERO LINO  
MMAWA MNGELO WA YEHOVA  
ANANDIYANKHULA NDIPO  
ANANDIENZA KUTI  
NDIKUTENGERENI KUNYUMBA  
KWANGA KUTI MUKADYE  
NDI KUMWA.




YEHOVA AKUTI: "CHIFUKWA SUNAMVERE  
LAMULO LA YEHOVA MULLINGU, KOMA WADYA  
NDI KUMWA KU MALO ANO, MTEMBO WAKO  
SUDZABWERERA KU YUDA KOTERO SUDZAIKIDWA  
KUMANDA KWA MAKOLO AKO."

NDADYA CHAKUDYA  
CHABWINO KWAMBIRI, KOMA  
NDIYENERA KUBWERERA KU  
YUDA TSOPANO.

ABABA,  
MUKUNENERA.  
KODI MULLINGU  
WAYANKHULA  
NANU?

INDE MWANA  
WANGA, PAPITA  
ZAKA ZAMBIRI  
NDISANANENER  
EPO.



AFADI, KOMA  
NDALAKWA NDINE.

MUKUTANTHAUZ  
A KUTI AFA?

1 MAFUMU 13:10-22



MNENERI UJA ANABWERERA  
MWANKHAWA, PODZIWA  
KUTI MULINGU AMACHITA  
ZIMENE WANENA. ANADZIWA KUTI  
AFA. KOMA SANKAYEMBEKEZA  
KUTI AFA POSACHEDWA,  
KOMANSO KUTI AFA BWANJI.






**AMENEYU NDI  
MNENERI  
WOCHOKERA KU  
YUDA!**

**NCHODABWITSANSO  
KUTI MKANGOWO NDI  
BULLU ZAKHALIRA PAMODZI  
PAMENEPO NGATI KUTI  
ZIKULONDERA  
MTEMBOWO.**

**SINDINAONEPO  
ZOTEREZI. MKANGO  
WAMUPHA KOMA  
MKANGOWO  
WANGOKHALA  
POMWEPO OSAFUNA  
KUDYA MTEMBO  
WAKE.**


MNENERI WONAMA UJA ANATENGA MUNTHU  
WA MULLINGU UJA NDIPO ANAKAMUIKA  
M'MANDA MWAKE PAMODZI NDI ANENERI A  
BAALA, PAFUPI NDI PAMALO PAMENE  
MULLINGU ANAONONGA GUWA LA NSEMBE.

MUNTHU WA MULLINGU  
UJA ANAIKIDWA M'MANDA,  
NDIPO POSAKHALITSA AMBIRI  
ANAMUIWALA. GUWA LANSEMBE  
LIJA ANALIKONZANSO NDIPO  
KWA ZAKA PAFUPIFUPI 300  
ANTHU OPEMBEDZA BAALA  
ANKAPEMBEDZERAPO, KOMA  
PALIBE AMENE ANATENTHA  
MAFUPA AO PA GUWA LA NSEMBE  
LIJA MONGA ANALOSERA  
MUNTHU WA MULLINGU UJA.

A man with a long white beard, wearing a blue robe, stands on the right side of the frame, facing a donkey. The donkey is facing away from the viewer, towards a set of stone steps leading up to a temple entrance. The temple has ornate columns and a golden doorway. The scene is set in a desert-like environment with a warm, golden light.

MULLINGU ADAMUKANTHA  
CHIFUKWA CHA KUSAMVERA  
KWAKE. ZOONA ZAKE NZAKUTI  
ZONSE ZIMENE MULLINGUYO  
ANANENA ZIDZACHITIKADI.

PAMBUIYO PAKE, PATATHA ZAKA 300,  
YOSIYA ANAKHALA MFUMU YA YUDA  
(640 B.C.). ANAPITA KU KACHISI  
NDIPO ANAPEZAKO KACHIDUTSWA  
KA BAIBULO. KACHIDUTSWAKO  
KADASALITSA MTIMA WAKE NDIPO  
ANAZINDIKIRA KUTI DZIKO LINAIWALA  
MULLINGU WAMOYO NDI KUMATSATIRA  
MAFANO. CHONCHO ANALAMULA KUTI  
AKULLUAKULU, ANSEMBE, ANENERI,  
NDI ONSE OKHALA MU YERUSALEMU  
ABWERE KUDZAMVA ZA M'BUKUMO.




ANTHUWO ANACHITA  
MANYAZI NDIPO  
ANAVOMEREZANA ZOMVERA  
MAU ONSE A M'BUKUMO.

1 MAFUMU 13:23-31; 2  
MAFUMU 21:24, 23:1-3



AMAI OYERA,  
TIPULLUMUTSENI!

ANTHUWO ANAMVERA  
MALAMULO A MULLINGU NDIPO  
ANAONONGA MAFANO ONSE  
M'DZIKOMO. ANAPHA ANSEMBE  
ONSE AMENE ANKAFUKIZA  
LUBANI KWA DZUWA, MWEZI,  
MLENGALENGA, NDI KWA  
MFUMUKAZI YA KUMWAMBA.



MALAMULO A MULLINGU, AMENE  
MOSE ANAPERKA, AMALESA  
MCHITIDWE WOTI AMUNA KAPENA  
AKAZI AZIGONANA OKHAOKHA,  
CHONCHO ONSE A MAKHALIDWE  
OTERE ANAPIRIKITSIDWA M'DZIKOMO.

ANTHU OLIMA  
MTIMA

ANAYERETSANSO DZIKOLO  
POCHOTSA ONSE AMENE  
ANKAFUNSIRA NZERU  
KWA MIZIMU,  
OBWEBWETA NDI MFITI.

PHWANYANI  
MPHIKA WAKEWO  
NDIPO  
MUTENTHE  
NYUMBAYO.

2 MAFUMU 23:5, 7, 10



ANAPHWANYA GUWA LA  
NSEMBE, ANAONONGA  
MAFANO ONSE, NDIPO  
ANAGWETSA MITENGO,  
NAPERA GUWALO  
KUKHALA NGATI FUMBI.

YOSIYA ANAPITA KU  
MALO OMWEWO  
AMENE MNENERI UJA  
ANAKUMANAKO NDI  
YEROBOWAMU, MFUMU  
YA UFUMU WA  
KUMPOTO, PATATHA  
ZAKA 300 TSOPANO.

*PALI MULUNGU  
MMODZI YEKHA NDIPO  
SAPEMBEDZEDWA KUDZERA  
M'MAFANIZO. ANSEMBE ONAMAWA  
ACHITITSA KUTI ANTHU  
AGALUKIRE YEHOVA!*





**MUYENERA  
KUFA BASI**

GUWA LANSEMBE LIJA  
LINANG'AMBIKANSO  
NDIPO PHULUSA  
LINATUKIRA KUNJA.

ANSEMBE ONSE ONAMA  
ANAPHEDWA NDIPO MATUPI  
AO ANAOTCHEDWA PA  
GUWA LOPHWANYIKALO.



PAFUPI NDI PA MALOWO  
PANALI MANDA A ANSEMBE  
ONAMA. POFUNA KUTI ANTHU  
ASAMAKAPEMBEDZE PA MANDA  
AO, YOSIYA ANAKUMBA  
MAFUPA AO NDI KUWATENTHA  
PA GUWA LA NSEMBE.


2 MAFUMU 23:15-16

**OTCHANI  
MAFUPA  
ONSEWO.**

**CHONCHO PATAPITA ZAKA  
300 ULOSI WAKALEWO  
UNAKWANIRITSIDWA, MONGA  
MOMWE MUNTHU WA  
MULLINGU ADANENERA.**

**NDIYE KUTI  
MUWASIYE  
MAFUPA AKE OKHAWO.  
TENTHANI ENAWO.  
KUPEMBEDZA MAFANO  
KOTERE KUYENERA KUTHA  
NGATI TIFUNA KUTI  
MULLINGU ATIDALITSE.**

**KOMA BWANA, MANDA  
AWA NDI A MUNTHU WA  
MULLINGU AMENE ANACHOKERA  
KU YUDA ZAKA 300 ZAPITAZO NDIPO  
ADALOSERA ZA TSIKU LINOLI. ADATI  
MUNTHU WOTCHEDWA YOSIYA, INU  
AMENE, ADZABWERA KUDZACHITA  
ZIMENE INUYO MWACHITA LERO LINO.**



WODALITSIKA  
NDINU, INU AMBUYE  
MULUNGU WATHU,  
MFUMU YA KUMWAMBA  
NDI PANSI, AMENE  
MUMAPEREKA CHAKUDYA  
KUCHOKERA M'NTHAKA.

TSOPANO KUPEMBEDZA MAFANO KUJA KUNATHA,  
NDIPO MFUMU YOSIYA ADALAMULA ANTHU ONSE  
KUTI AZISUNGA PASKHA POKUMBUKIRA YEHOVA,  
AMENE ANATULUTSA MAKOLO AO M'DZIKO LA  
IGUPTO NDI KUWAPATSA DZIKOLO.

2 MAFUMU  
23:17-18, 21-22

ATATE, NCHIFUKWA  
CHIYANI TSIKULI NDI  
LOSIYANA NDI MASIKU  
ENA ONSE?

CHONCHO ATATEWO ANAWALIZA MBIRI YAKALEKALE,  
MMENE MULLINGU ANAWAPULUMUTSIRA MU UKAPOLO  
M'DZIKO LA IGUPTO NAWAPATSA MALAMULO NDI  
CHHEMA. ANAWALIZA MMENE MAGAZI OPAKA PA ZITSEKO  
ANAPULUMUTSIRA ANA AAMUNA OYAMBA KUBADWA KWA  
MNGELO WOONONGA. INALI PASKHA YAIKULU KWAMBIRI.





<https://goodandevilbook.com/>